



Yerusalemu Watsopano

Matchalitchi Dziko Lonse

Mbusa Tony Alamo

Fuko La Chikhristu La Alamo

Volume 20500

NJIRA YOKHAYO YOCHOKERA

Wolemba Tony Alamo

Mbewu imene MULUNGU anauza Abrahamu kuti idzadalitsa mafuko onse inali mbewu imene inali ndi moyo wosatha mwa iyo (Genesis 12:3). Mbewu zonse zili ndi moyo wochepa mwa izo, koma mbewu imodzi yokha ili ndi moyo wosatha mwa iyo, ndipo "mbewu imeneyi ndi MAWU a MULUNGU," amene ali YESU (Luka 8:11).¹ YESU

ndi mbewu yokhayo komanso ndi odzala wa mbewuyo, MAWU a MULUNGU (Luka 8:5-15). Ife amene tili kachisi wa MULUNGU ndi thupi la KHRISTU, mkwatinibwi WAKE, tili ndi YESU ndi ATATE mwa MZIMU amene akhala mwa ife, kotoero ife mwa MZIMU takhala ofesa mbewu za moyo wosatha, zimene zilinso KHRISTU, MAWU (Yohane 4:36).²

Komanso, ndife oitanidwa-adziko-lapansi, tchalitchi.³ Komanso, mbewu, YESU, ndi MAWU a MULUNGU. Ife, olungama, oitanidwa-adziko-lapansi, tchalitchi—zonsezi ndi moyo, moyo wosatha, umene uli mbewu yosafa ndi, komanso, ndiyo MAWU a MULUNGU, amene ali MULUNGU amene anakhala munthu ndikukhala nafe pansi pano, EMANUELI, kutanthauza kuti MULUNGU nafe (Mateyu 1:23).



Tony Alamo ku manzere ndi osinthika atsopano oti abatizidwe mchaka cha 1970

Ena opusa amati, "Chabwino, ndi kudziwa sindimawerenga Baibulo monga ndikuyenera kuchitira," pogoniza kuti mawu opusa amanenawa ndi njira yodzichepetsera ndi kudzitsitsa, kuulula mwachilungamo, ndipo kuti adzapulumuka pakunena zinthu zogwetsa ulesizi. Komabe, akungodzipweteka okha kosalekeza. Chomwecho "chikhulupiliro chidza ndi mbiri, ndipo mbiri idza mwa MAWU a MULUNGU," amenenso ali mbewu, chinthu chokhacho chimene chili ndi moyo wosatha mwa icho (Aroma 10:17). MAWU ndiye MULUNGU (Yohane 1:1). MULUNGU ndi wamuyaya, kotoero ngati MULUNGU ali mwa inu mwa ubwino wa MAWU, simudzafa, ngati mun-gakhanzikike mpaka ku chimaliziro.⁴

China chili chonse tikuchiona padziko lapansi chinaukitsidwa ndi

MAWU a MULUNGU kuchoka ku dziko lapansi, kuti tithe kuona bwinobwino, makamaka kwa ife amene timamudziwa MULUNGU kapena takhala tikumudziwa IYE.

"Pakuti mkwiyo wa MULUNGU waonekera kuchokera Kumwamba kutsutsana ndi zonse zopanda umulungu ndi chilungamo za anthu, amene akakamiza pansi choonadi

m'chosalungama chawo; Chifukwa chodziwika cha MULUNGU cha-onekera mkatи mwawo; pakuti MULUNGU anachionetsera kwa iwo. Pakuti zinthu zosaoneka za IYE kuy-ambira nthawi imene analenga dziko lapansi zikuoneka bwinobwino, kuzindikiridwa ndi zinthu zimene zinalengedwa, ngakhale mphamvu YAKE yosatha ndi UMULUNGU wake; kuti iwo akhale opanda mawu akuwilingura; Chifukwa kuti, akamudziwa MULUNGU [osiya chi Khristu], anamulambira IYE osati ngati MULUNGU, ndipo sanamuyamike; koma anakhala opanda pake m'maganizo awo, ndipo mtima wao wopulukira unada. Pakunena kuti ali a nzeru, anapusa, nasandutsa ulemelero wa MULUNGU wopanda chinyengo kukhala fanizo la munthu

(Yapitirira patsamba 2)

¹ Mat. 4:3-4, Yoh. 1:1, 14, 1 Yoh. 1:1-3, 5:11, Chiv. 19:13 ² Mark 16:15-16, 1 Ako. 1:21-24, 6:19, 2 Ako. 5:17-21 ³ Yoh. 15:16, 19, 17:6, 14-16, 2 Ako. 6:14-18, 1 Pet. 2:9 ⁴ Mat. 4:4, 10:22, 24:13, Yoh. 5:24, 6:63, 11:26, Mac. 14:22, Aro. 11:22, Ako. 1:22-23, 1 Tim. 4:16, 2 Tim. 2:1-3, 3:13-17, 4:5, Yak. 5:10-11, 1 Yoh. 2:24-25

NJIRA YOKHAYO YOCHOKERA

(Yachokera patsamba 1)

wachinyengo, ndi kwa mbalame, komanso nyama za miyendo inayi, ndi zinthu zokwawa.

"Chifukwa chake MULUNGU anawapereka iwo ku zonyansa kudzera m'zilakolako zamitima yawo ya chiwerewere, kunyazitsa matupi awo pakati pawo: Amenewo anasandutsa choonadi cha MULUNGU kukhala chabodza, napembedza ndikutumukira cholengedwa kuposa Mlengi, amene ali wolemekeze ka ku nthawi yosatha. Amen. Chifukwa cha ichi MULUNGU anawapereka iwo ku zilakolako za manyazi: pakuti angakhale akazi awo anasandutsa machitidwe awo a chibadwidwe kukhala machitidwe osalingana ndi chibadwidwe: Chimodzimodzinso amuna, anasiya machitidwe a chibadwidwe cha akazi, natenthetsana ndi chilakolako chawo wina ndi mzake; amuna okhaokha anachitirana chamanyazi, ndipo analandira mwa iwo okha mphoto yakuyenera kulakwa kwavo [chiyenerero].

"Ndipo monga iwo anakana MULUNGU mwakudziwa kwavo, MULUNGU anawapereka ku mtima wokanika, kukachita zinthu zosayenlera; Anadzadza ndi zosalungama zonse, chisembwere, kuipa, kusilira, dumbo; odzala ndi kaduka, mbanda,

mtsutso, chinyengo, udani; akazitape, osinjilira, adani a MULUNGU, achipongwe, odzitama, amatukutuku, oyamba zoipa, osamvera makolo, opanda nzeru, osasunga mapangano, opanda chikondi cha chibadwidwe, osakhutitsidwa, opanda chifundo: amene ngakhale adziwa kuweruza kwake kwa MULUNGU [chifukwa anapulumutsidwapo nthawi ina], kuti iwo amene achita zotere ayenera imfa, azichita iwo okha, ndiponso abvomerezana ndi iwo akuzichita" (Aroma 1:18-32).⁵

Dziko lapansi tsopano labwelerango kukhala ngati dziko lomwe lija la masiku a Noah (Genesis 6:5-7, Matthew 24:37-44). Maganizo a anthu lero asintha choonadi cha MULUNGU kukhala chabodza (Aroma 1:21-25).⁶ Choonaadi cha MULUNGU ndikuti IYE ndi mbewu yokhayo imene ili ndi moyo wosatha mwa IYE. Tsopano akunena kuti, monga anachitira m'nthawi ya Nowa, kuti choonadi ichi cha MULUNGU kukhala mbewu yokhayo ya moyo wosatha ndi bodza, ndipo akuphunzitsa ana athu zoipazi, zachinyengo, mphulupulu zopweteketsa moyo kwambiri m'masukulu onse aboma. Zisokwanira kwa iwo kukwatirana wina ndi mzake. Akufuna kuhunzitsa ana athu kuti choonadi cha MULUNGU ndichabodza. Anavomereza ziwanda (ziwanda za chiwerewere cha pakati pa amuna okhaokha kapeza aka-

zi okhaokha, umathanyula) mwa iwo, ziwanda zamphamvu zimene zikuwapangitsa kulambira zinthu zimene zili zopatsa chilakolako cha chiwerewere, koteru amatumikira fano kuposa Mlengi (Aroma 1:25). Chifukwa cha ichi, MULUNGU waasiya. IYE waalekelera kuchita zoipitsitsa, kuchita zoipitsitsa zavo, zimene amakonda kwambiri. MULUNGU amaona momwe am'kanira IYE ndi moyo WAKE wosatha, ndipo mwa mwano amalimbana NAYE pa chifukwachi, ndipo MULUNGU anangowasiya. MULUNGU anawasiya iwo kukhala ndi zinthu zimene akufuna, zimene zili zoipitsitsa! IYE anawalora iwo kuchita zimene asankha kuchita—akazi ndi akazi, amuna ndi amuna, kugonana kwa pakati pa akazi okhaokha ndi kugonana kwa pakati pa amuna okhaokha.

Nigeria

Okondeka M'busa Tony,

Moni kwa inu mu dzina la Yesu. Ndine okondwa kukudziwtsani kuti ndakhala kale mtumiki wa Mulungu kudzera m'mabuku a uthenga wabwino amene ndinawerenga komanso porogaramu yanu ya pa Radio Africa. Ndikukuthokozani ndi m'mene mukuulutsira Mau a Mulungu kwa ife kuno. Ndine wongosynthika kumene ndipo ndikufuna munditumizire Baibulo Lopatulika lathunthu ndi makalata a nkhanu pamodzi ndi mabuku a Messiah. Ndinali wosochera ndipo ndapezekanso.

Ambuye adalitse utumiki wanu koposa. Ndikhulupilira kuti ndimva kuchoka kwa inu posachedwa. Wanu Mokhulupirika, Mone Akinwa and family Sunshine State, Nigeria



M'busa P.V. Ratnam
kugawa zolemba
za Pastor Alamo
m'mudzi wa Andhra
Pradesh, ku India



MAUTUMIKI A ALAMO PA INTANETI
www.alamoministries.com

Komabe, mbewu ya MULUNGU, mbewu ya moyo wosatha ya MULUNGU, siingakhale m'moyo wa munthu oipitsitsa, chifukwa ichi chimasintha choonadi cha MULUNGU kukhala bodza! Chiwanda ichi chogonana akazi okhaokha kapena amuna okhaokha ndi champhamvu, koma YESU, mbewu ya moyo wosatha mwa IYE, ndi yamphamvu koposa.⁷ MULUNGU amatiuza kuti tim'kane mdierekezi ndipo adzathawa ife (Yakobo 4:7).⁸ Koma boma la dziko lapansi likuta ngati tikana kugonana akazi okhaokha kapena amuna okhaokha, tikupalamula mlandu wachidani.

⁷ Det. 4:39, 32:39, 1 Sam. 2:6-8, 1 Mbi. 29:11-12, 2 Mbi. 20:6, Mas. 46:1, Yes. 44:6, 45:23, Yer. 10:10, 18:6, Dan. 4:35-37, Yoh. 10:29, Mac. 17:24-26, Chiv. 1:12-18 ⁸ Mat. 4:1-11, Aro. 12:9, Aef. 4:27, 53:17, 1 Ate. 5:21-22 ⁹ 1 Mbi. 28:9, Yobu 4:7-9, 21:14-20, Miy. 1:22-32, 8:36, 10:25, Yes. 1:15-20, Dan. 12:2-3, Luka 12:4-9, Yoh. 3:16-21, 36, Aro. 1:18, 1 Ako. 6:9-10, Yuda 14-15, Chiv. 20:11-15, 21:8, 27 ¹⁰ Mat. 24:11-12, 24, 1 Tim. 4:1-2, 2 Tim. 3:13, 2 Pet. 2:1-3, Chiv. 13:1-4, 11-15, 14:8, 17:8, 18:2-3, 23

Congo

(Zomasuliridwa kuchoka kuchi Faransa)

M'busa wa dziko lonse Tony Alamo,

Mtendere mwa Khristu! Ndine M'busa Andre Hilarion, m'modzi mwa okonda kwambiri kuwerenga nkhani zanu za m'makalata. Makamaka munali mu 2006 m'mene ndinazindikira za zolemba zanu zosindikizidwa ndipo zinasinthiratu utumiki wanga. Chifukwa Mzimu Woyeru unanditsegula maso pamene ndinaziwerenga. Pachifukwa ichi, pa tchalichi pomwe ine ndili m'busa, tsopano tikugwiritsa ntchito zolembewazi "Chinsinsi cha Papa" ngati chida chopelekera umboni m'malo opeze-kera anthu, ndipo Ambuye tsopano akuchita zinthu zazikulu. Sabata iliyonse tikumalandira anthu atsopano omwe akumagwidwa ndi Mzimu Woyeru akatha kuwerenga ndikuchilandila, popereka mitima yawo kwa Yesu ndikuyamba moyo watsopano.

Tsopano, chomwe tikupempha ndi chakuti muzititumizila makalata ambiri moseakeza ndi nkhani zamu chiFaransa zomwe zidzatithandize kukhanzikitsa malo ogawilira zolembewazi za M'busa Tony Alamo.

Kotero, M'busa Tony Alamo, Mulungu wanu ndi Mulungu wathu. Cholinga chanu chakhala cholinga chathunso. Ndipo nkhondo yanu ndi nkhondo yathunso. Tikuthokozelatu, ndipo tikupemphera kwa Mulungu wa Mphamvu zonse kuti mupitilirebe kukhala njira ngati m'dalitso wathu komanso wa anthu a mitundu ina yonse. Andre Hilarion

Kimpese, Democratic Republic of the Congo

Missouri

Okondeka M'busa Tony Alamo

Ndili oyamika chifukwa cha utumiki wanu ndi chibvumbulutso cha choonadi chomwe Mulungu anakupatsani. Mwanditsekula m'maso m'choonadi ndi-kulimbikitsa chikhulupiliro changa mwa Mulungu, mwandiululira zinyengo za Satana, boma la maiko onse, ntchito zake zosutsana nafe, Mkwatibwi, ndi zonse zomwe amagwiritsa nthito mu dziko losocherali.

Chonde nditumizireni zipangizo zonse zimene mungakwanitse kundipatsa. Ndikuzifuna ZONSE. Zikomo kwambiri ndipo Mulungu Wamoyo akudalitseni ndi utumiki wanu kopambana mu chisomo ndi mphamvu Zake!

Chonde tuyike dzina langa pa m'ndandanda wa mapemphero anu.

Mwa Khristu,
Terry Birmingham

YESU asanakwerenso Kumwamba, IYE anali atagonjetsa imfa, Gehena, manga, Satana, ndi ziwanda zonse zoipitsitsa, koma aliyense wokana moyo wosatha adzalandira mphotho chifukwa cha maganizo awo oipa.⁹ Adzalandira mwa iwo okha mphotho yakuyenera kulakwa kwao imene ili Gehena ndi Nyanja ya Moto, kuzunzika kosatha. Akuchita izi kwa iwo okha monga kunakhala masiku a Nowa (Luka 17:26-30).

Chakhala chizolowezi kutsatira Satana, amene wanamiza dziko lonse lapansi (Chivumbulutso 12:9).¹⁰

Zomwe ofalitsa uthenga ndi boma akuchita zikupangitsa MAWU a MULUNGU kukhala mlandu wa chidani, koma ndi moyo okhawo komanso njira yokhayo yothawira ku mazunzo ndi nkhanza zosatha ku Gehena ndi Nyanja ya Moto. YESU ndi anthu AKE ndiokhawo amene asamala za moyo wako. Osalora mzimu wa Satana kukupusitsani. Simunabadwe choncho. Chiwanda chikhonza kukulowani momwe munali mwana wamng'ono kwambiri, koma YESU amachotsa zi-wanda mwa anthu.¹¹ IYE ndi MOYO ndipo moyo wochuluka.¹² "Ndadza ine kuti akhale ndi moyo, ndikukhala nao wochuluka" (Yohane 10:10).

Nditati ndikuonetsani inu momwe mungathawire chilango cho-satha, mukhonza kukhulupilira kuti uwu ndi mlandu wa chidani. Moyo kuno ndiwaufupi, koma muyaya

(Yapitirira patsamba 4)

¹¹ Mat. 8:16-17, 28-34, 9:32-33, 10:1, Marko 1:34, 39, 7:25-30, 9:17-27, 16:9, Luka 11:14 ¹² Yoh. 11:25-26, 14:6

India

Okondeka M'busa Tony,

Ndinapita kumudzi kwa bambo anga kotchedwa Sandipudi masiku khumi apitawo kukaona nyumba yathu yakale. Ndipo kunali okhulupilira odwalika kwambiri atagona pa bedi lake anthu nkumaganiza kuti mwina wamwalira, koma ndinapita kukamuona ndi kukamupempheler. Mulungu anamva mapempherowo ndipo anamuchiritsiratu. Kudzera munjira imeneyi mseu onse unandipatsa ulemu kwambiri, koma ndi-nakhulupilira ndipo ndinanena kwa iwo, "Si ine, koma Yesu ndi amene wachita izi. Tiyen'i timutamande ndi kumupatsa ulemu lye."

Ndikhulupilira kuti mapemphero anu aphindu anandithandiza mu utumiki Wake. Tiyen'i timulemekeze lye kudzera m'machitidwe komanso m'mawu.

Ndikukuthokozani nonse. Chonde ndipempherereni ndi zolina zathu koposa.

M'chikondi chake,
M'bale wanu,
Rajesh Tatapudi
Andhra Pradesh, India

NJIRA YOKHAYO YOCHOKERA

(Yachokera patsamba 3)

ndi wautali.¹³ Siumatha. Mizimu ya anthu idzakhala ndi moyo wosatha Kumwamba kapena ku Gehena.¹⁴ Tonse ndife anthu. Tonse tinapatsidwa ufulu osankha moyo kapena imfa, chabwino kapena choipa, MULUNGU kapena Satana.¹⁵ Pamene MZIMU wa MULUNGU wakulowani ndipo inu ndikusunga IYE pakumulandira IYE, MAWU AKE, tsiku lili lonse, inu mudzakanitsa kukhala ndi mphamvu-ymoyo WAKE mwa inu ndi mphamvu YAKE kufikira inu mudzafe. Komabe, khama lonse liperekedwe pa ichi. Satana sakusewera nanu! Akufuna inu mukakhale ku Gehena ndi Nyanja ya Moto ndi iyeyo.

MULUNGU sakusewera, nayenso. IYE anatifera pamtanda wa Kavari, kenako anauka kwa akufa ndikukwera Kumwamba kutitsimikizira ife kuti IYE ndi MULUNGU ndipo kuti ali ndi

mphamvu zotipulumutsira ndikutiukitsanso ife pa tsiku lomaliza.¹⁶

Chikondi si chiwerewere. Chikondi ndikusunga malamulo a MULUNGU (1 Yohane 5:3).¹⁷ Mukatero, mudzakhala ndi moyo. YESU anati munthu wakunena kuti andidziwa INE (andikonda INE) koma osasunga malamulo ANGA ali wabodza, ndipo mwa iye mulibe choonadi (1 Yohane 2:4). “Ndipo monga iwo anakana kukhala naye

MULUNGU m'chidziwitso chawo, MULUNGU anawapereka ku mitima yukanika” (ndi ku m'chitidwe wawo wokanika), kukachita zinthu zimene Satana akufuna iwo azichta, ndipo mzimu wake woipa mwa iwo umawapangitsa iwo kuvomer-eza kuzichita (Aroma 1:28-32).

Asiyeni opusa akhale mafumu ndikulamulira dziko ndi golide, mphulupulu, ndale, ndi zinthu zina, koma

(Yapitirira patsamba 8)

16 Marko chap. 16, Yoh. 11:25-26, Mac. 2:29-33, 4:10-12, 1 Ako. 15:3-22, 1 Pet. 1:3-5 **17** Eks. 20:6, Det. 7:9, 11:1, 13-15, 30:16, Yos. 22:5, Yoh. 14:15, 21, 15:10, 2 Yoh. 6

Arkansas

Okondeka M'busa Tony,

Lero ndinali ndi mzanga amene ali m'Khristu wobadwanso mwatsopano. Analu kumaliro. Mzibambo amene anamwalira analu m'busa, ndipo panali anthu ambiri pa maliro ake. Umboni wake asanamwalire unali wakuti kulikonse kumene adzapite, adzakhala akuuza anthu nthawi zonse, kaya ndiku Walmart kapena m'sitolo ya mankhwala kapenanso pamsewu, “Kodi mumamudziwa Yesu Khristu ngati Mpulumutsi wa moyo wanu? Muli m'chiyero ndi Mulungu?” Anachita izi pali ponse pamene amapita, mpaka anthu ena ankadabwa chifukwa chake ankachitira izi.

Ndithu, ku maliro, mwana wake wamkazi anayima ndikunena kuti, “Ndikufuna kukuuzani nonse nkhanu ya bambo anga. Ndili wamng'ono, ndili ndi zaka pafupifupi 13, ndimakonda kupita nawo nthawi zambiri, ndipo kuli konse komwe timapita amaima ndikufunsa wina wake ngati analu bwino ndi Yesu, kapena ankanena kuti, ‘Kodi ukumudziwa Yesu Khristu ngati Mpulumutsi wa moyo wako?’ Panali nthawi zina zimene ndimaona ngati ankaonjeza. Amatha kuuza aliyense, ndipo ankangopitilizabe.

“Tsiku lina tinalowa mu galimoto ndipo ndinati, ‘Bambo, ndi chifukwa chiyani mumauza aliyense za Yesu?’ Bambo anga anati, ‘Mwana wanga, ndi kuuza nkhanu. Ndinali ndi masomphenya a maloto pamene ndinali ndi zaka

17, ndipo m'masophenyawo ndinamwaliramo ndi kupita Kumwamba. Analu malo okongola kwambiri kuposa onse. Kenako ananditengera ku mphepete kwa Kumwamba, ndipo ndinayang'ana pansi mu Gehena. Ndinaona manja atakwenzedwera kwa ine ndipo amakuwira pa ine, “N'chifukwa chiyani sunatiuze! N'chifukwa chiyani sunatiuze!” Ndipo analu anthu amene ine ndimawadziwa. Maloto anatha ndipo ndinabwelera pano pa dziko lapansi ndipo ndi chifukwa chake ndimauza aliyense.”

Mzanga ananena kuti zinamukumbutsa zambiri za ife, ndi zolemba za M'busa Alamo, chifukwa kuli konse komwe tingapite, timakhalala tikugawa zolembedwa nthawi zonse. Ananena kuti M'busa Tony wakhala akuchenjeza anthu kwa zaka ndi zaka.

Alemekezeke Ambuye,
M'bale Tommy

Kenya

Moni M'busa Tony Alamo,

Ndadziehetepeta chifukwa chakukhudzidwa kwanu. Ndinadalitsika kwambiri ndi kalata yanu ya nkhanu “Ndinam'peza Yesu pa webusaiti ya Tony.” Ndinayiwerenga nkhanu ndipo ndinanena pemphero lopempha chikhululuko pa kalata ya nkhanu. Ndinapiratu machimo anga, ndipo ndinasunthidwa mpaka misonzi pamene ndimanong'oneza bondo panthawi yomwe ndinataya m'dzikio kunyoza Mulungu! Ndinamva kupepkidwa katundu olemtsa wa machimo atachoka mwa ine. Zoonadi ndikumva kupepkidwa ndi kumasulidwa. Oh, ndithudi ndinkasowa chisangalalo choterochi, chisangalalo chokhulukidwa machimo, chisangalalo chokhala mwa Khristu. Ndikuthokoza AMBUYE populumsa moyo wanga ndipo ndikupemphera kuti MZIMU WOYERA undiyang'anire munjira iyi ya uzimu. Tsopano, ndine ongoyamba kumene mu ulendo wa uzimu. Chonde ndiyang'anireni mmene ndizichitira ndikuchititsa manyazi mdierekezei ndi bodza lake. Ndikubwerenzanso kuti ndikuyamika mautumiki anu pamene akupereka chili chonse chokhudzana ndi uzimu. Mulungu akudalitseni kopambana inu pamodzi ndi mautumiki anu.

Sarah Terry

Bungoma, Kenya

Kuchokera ku Nthambi yathu Yomasulira Mawu

Tikugwira ntchito yomasulira Ilacono (chiyankhulo choyankhulidwa ku Mpoto kwa Phillipines), ndipo m'modzi mwa omasulira ndi wachinyamata amene analeledwa Pentekosto, anatsiliza maphunziro ake a zauzimu ku seminale (theological seminary), ndi kuphunzitsa pa sukulu ya Baibulo ya ana. Tchalitchi chawo chili ndi matchalitchi ena 50 amene anamwazikana ku Mpoto kwa Phillipines konse, chili chonse ndi M'busa wakewake. Panopa akugwira ntchito ndi American Bible Society kumasulira ndemanga za m'Baibulo ndi kuthandizira buku lili lonse la Baibulo.

Anatiuza kuti pamene anaona za umwinimwini (copyrights) pa "Chinsisi cha Papa," "Papa Wothawa Mlandu" "Yesu Anati Satana akadakhala ndi Tchalitchi komanso Boma," ndi "Mfumukazi ya Mahule," anaona kuti zinali zoti zinalembeda m'zaka za ma 80 ndi 90. Anati ndizoziwitsa kuti M'busa Alamo analemba mfundozi kalekale, ndipo pa nthawi imeneyo palibe yemwe ankaona kuti ndi zonna, koma pano mutha kuona mosavuta. M'busa Alamo anadziwa zinthuzi wina aliyense asanadziwe ndipo anazisdikiza kuti achenjeze aliyense.

Iye anati Phillipines ndi ya Katolika kwambiri sungamuuze munthu za Ambuye, koma atawerenga makalata a anthu

opempha zolembeda kuti azigawa ndi kuchitira umboni kwa anthu, anapempha zolembeda 100 pa gavo lili lonse la zomwe zinalembeda zomwe anathan-diza kumasulira kuti akagawe. Anayitanitsano bandulo ya mabuku a Mesiya. Iye anati, "Ndimamasulira zaku Bible Society, koma izi ndi zokopa miyoyo." Iye anati ndiosangalala kukhala gavo la izi, ndipo akugwiritsa ntchito zolembedwazi m'makalasi ake. Iye anati, "Ndakhala ku seminare ndipo zili mwa ine, koma zolembewazi ndi zonna komanso ndi zofunikira kwambiri. Ndikutha kuona kufunikira kwa zimene zikuchitika pano m'moyo mwanga. Ndikuona zolembewazi ndi zimene zikuchitika pano."

Omasulira m'chi Swahili ndi mayi wa ana atatu yemwe mwamuna wake ndi m'busa. Iye anati amayenera kukhala wachilungamo, kuti mmene amagwira ntchito pa magawo a zolembeda zosiyanasiyana okhudza Papa, ankaganiza kuti zina mwa zomwe ankamudzudzula Papa ndi Tchalitchi cha Katolika zinali zongopeka ndi zongoganizira. Anati amadziwa kuti chiKatolika chinali chiphunzitsa chabodza, koteri choonadi cha mauthenga

analibe nacho ntchito nabola anthu amachikana. Komabe, sankakhulupilira.

Iye anati mamuna wake ankawerenga zolembewazi usiku wina ndipo anafunsa, "Ndi chifukwa chiyani unayitanitsa izi?" Anati kwa iye, "Kuti ndikagawe kwa anthu ndikapita ndi ana ku paki." Nthawi yomweyo anati, "Ayi ndithu! Uzisunge izi! Sungakangozigawa zimenezi. Izi ndi zoona! Tiyenera kuziwerenga." Anati, "Ndinapita ku koleji ya Baibulo ndipo zinthu izi zimaphunzitsidwa ndi kulembewa ndipo zonse zalembewazi ndi zonna."

Iye anati anamuyang'ana mwamuna wake ndipo anayankhula chamumtima, "Unapita ku koleji ya Baibulo zaka zapitazo ndipo umadziwa zinthuzi kuti ndi zonna. Ndi chiyani iwe kapena koleji munachita kuchenjeza dziko lapansi? Iwe ngakhale ali yense palibe amene anachitapo kanthu za izi. Bambo uyu (M'busa Alamo) anaitanidwa mwa padera ndi Mulungu kuti ayankhule chifukwa iwe ngakhale ali yense simunatero kapena simukutero."

Omasulira waku Sweden analeredwa Purotestanti, koma kwa zaka zambiri wakhala alibe nazo ntchito za tchalitchi, mpingo, kapena Mulungu. Ndi oona za ndale, olimbana ndi zolakwika zosiyanasiyana m'boma la Sweden. Amalemba ma bulogu a zandale ndipo amakhala ndi misonkhano komanso amamasulira zolembeda mwa padera. Amavomereza kwambiri zikhulupiliro zake, koma akuwerenga kanusu kotengedwa m'bukhu la Mesiya, anayamba kulira atawerenga, "Gulu linafuula, 'Mpachikeni Iye, Mpachikeni Iye."

Iye anatiuza kuti, "Ndaphunzira njira za ziwebu (conspiracy theories), koma sindinaonepo aliyense akugwiranitsa zonse ku Vatican ngati chonchi. Izi ndi zodabwitsa. Ndkukonda ndithu kuchita ichi. Nonsenu mwayamba kundipatsa chikoka. Ndimalemba bulogu yanga ndipo ndinan-gonna ndikutchula za Chivumbulutso."

Omasulira waku Serbia, yemwe ali ndi digri ya batchala mu history, anati ndi zosangalatsa kutengapo mbali pa izi. Anati Serbia ili ndi mbiri yovuta kumvetsa yokhudzana ndi nkhanza za chipembedzo ndi kuphana kwambiri, ndipo M'busa Alamo akuvutika ndi mazunzo okhudza chipembedzochi ndipo akulankhulabe. Iye anati zimenezi ndi zosangalatsa.

Nigeria

Okondeka Mpingo wa Alamo,

Landirani moni mu dzina lodalitsika la Ambuye ndi Mpulumutsi wathu Yesu Kristu. Kalata ya nkhani ya dziko lonse ya Tony Alamo Christian Ministries ikusintha miyoyo ya mzinda wa Igodan Lisa ku Nigeria. Kudzodza kwa kalata imeneyi ndi kwakukulu kwambiri. Yathandiza moyo wanga wauzimu pondis-unthira malo ena otha kumvetsa zinthu za Mulungu. Analu ogawa makalata wanu amene anandipatsa kalata yanu ya nkhani yotchedwa "Chivomelezi." Ndinapezeraponso mwayi opatsa anthu ena ndipo kwa onse amene ndinawapatsa pepala, analandira Yesu kukhala Mbeye wa moyo wao. Ulemelero, matamando akhale kwa Mulungu.

Chonde ndikupempha kuti mutitumizire zambiri, kuti atithandize kukopa miyoyo yambiri. Mulungu adalitse ntchito zanu. Zikomo.

Wanu mwa Khristu,
Jasaau Imamu

Ondo State, Nigeria

New York

Okondeka M'busa Tony Alamo,

Ndinalandira kalata yanu ya nkhani m'njira ya sitima ya panjanji ypyenda kunci kwa nthaka (subway) ku New York, ndipo inandipeza nthawi yomwe ndinkafuna thandizo kwambiri. Uthenga womwe uli m'zolembeda zanu ndio-funikira kwambiri.

Ndikupemphanso buku lanu lotchedwa Mesiya, nkhani za m'makalata 100, komanso mauthenga a pa CD.

Zikomo,

Eric F.

Rhinebeck, NY

Umboni Wamachiritso

(Yotanthauzidwa kuchokera ku Chipwitikizi)

October 27, 2014

Dzina langa ndine M'busa Isaue Roberto. Ndimachokera ku Londrina m'boma la Paraná, Brazil, ndipo ndiku-funa kugawana nanu chinachake kudzela mu imelo imeneyi. Ndakhala ndili m'busa ku Londrina kwa zaka 15. Zaka zitatu zapitazo banja langa lin-awopsezedwa ndi ngozi, koma inali yayikulu.

Pa 24 July, 2011, mwana wathu wamkazi Beatriz Gabriella (ali ndi zaka zisanu ndi ziwiri), anachita ngozi yoopsa ya galimoto pomwe anagundidwa ndi dalaivala wa takisi pamene ankadutsa powolokera msewu. Anagundidwa mwa mphamu moti, malingana ndi azakafukufuku, anaponyedwa mtunda okwana mafiti 21. Ndinathamangira pomwe anali, samapuma, ndipo ndiku-kumbukira ndinakuwa, "Wina aitanitse chithandizo!" Ndityayang'ananso pomwe anali iye, ndinaona njinga ya moto ndi mau omwe anati, "Ndithandiza. Ndine ozimitsa moto." Nthawi imeneyo, Mulungu anabweretsa oyankha oyamba pamenepo. Anamutembenuza Beatriz ndikumugonetsa chagada kenako anamupanga CPR, ndipo anatsokomola magazi. Thandizo linafika, ndipo pomwe amamuthandiza mkatì mwa ambulasi, ndinayamba kupemphera. Satana m'dyelekezi ankandilondalonda ndipo anandiwonetsa mumtima mwanga chithunzi cha m'nyamata yemwe ndinkamudziwa yemwe anagundidwa ndi galimoto ndipo anasiya kuyankhula ndi kupanga zolongosoka. Tsopano banja lake limamuyendetsa pa njinga ya olumala, whilutcheya. Nthawi imeneyo, m'dyelekezi ankandibweretsera chithunzi chake ndikumati, "mmenemo ndimmene mwana wako adzakhalire."

Anamutengera kuchipatala ndipo anagonekedwa atamu-peza ndi mavuto awa: mwen-do wakumamzere wothyoka,



mkono wakumamzere wothyoka, chidale chakumamzere ndi chakumanja chinathyoka, chiwalo cha mmimba (spleen) chovulala, mapapo anaonongeka komanso kusokonezeka kwa mutu kwa level 3. (Level 4 ndi imfa).

Titafika ku malo osamalira odwalika kwambiri (Intensive Care Unit), tinaona mwana wathu atalumikizidwa ku zida zambirimbiri, amapuma mothandizidwa ndi makina, ndipo atakomo-

ka. Patapita masiku atatu chipangireni ngozi, pa 27 July, dotolo (neurosurgeon) yemwe ankamuthandiza anatiyitana ndikutiua kuti, "Ndili ndi nkhanu yosakhala bwino. Mmene analili zikupitilira kuyipilayipila. Mankhwala sakugwira nthito kwa Beatriz, ndipo bongo wake sulibwino. Ubongo ukutupa. Chifukwa cha ichi, magazi sakuyenda bwino kudutsa mu bongo, ndipo m'mawola ochepa akudzawa, ubongo wa Beatriz usiyiratu kugwira ntchito," Dotolo anati. "Ndili ndi njira ina imodzi yomaliza, yomwe ndikupanga sajare kuti tichotse chidutswa cha chigaza mbali zonse kuti tichepetse mphamu mubongo wa Beatriz, ndicholinga choti papezeke malo oti bongowo uzifufumilapo. Komabe, palibe chitsimikizo choti angasinthe kapena kulimba ndi sajareyo."

Tinavomereza zomupanga sajare, chifukwa tinadziwa kuti mawu wot-

siriza mwini wake ndi Mulungu. Pamene amakonzekera zonse, anatiuza kuti tikhale ndi Beatriz kuti tithe kutsanzikana naye. Mkazi wanga anayamba kupemphera pamene ine ndinawaitana othandiza kupemphera ndikuwalongosolera mmene zinthu zinaliri. Pamene mkazi wanga anasamira thupi la Beatriz akupemphera, munthu wina anabwera kwa iye nati, "Mai, ndikukulangizani kuti mungopemphera kwa Mulungu kuti angomutenga, chifukwa ngakhale achire, azidzangokhalira kugona pa bedingati chipukupuku." Patapita maola angapo, ndisakudziwa chomwe chinachitika, ndinalandira uthenga pa foni kuchokera kwa mlamu wanga wakuti amapemphera masana ndipo anaona masomphenya. Anaona mzymu oipa utabwera kwa mkazi wanga ndikun-ena ndendende mau omweo.

Sajare inatenga pafupifupi mawola asanu. Mmene amamubweretsa Beatriz ku malo osamalira odwalika kwambiri, mutu wake unali utakutidwa wonse komanso nkhopo yake itasinta. Tsopano ndinkangodikilira. Tinapemphera kuti Mulungu amuchiritse, koma nkhanu zoipa zink-abwerabe—chibayo, matenda owa-tenga kuchipatala konko.

Tsiku lina lisanafike tsiku lomwe Beatriz anabadwa (8 August), dotolo anati asiya kumupatsa makhwala oletsza ululu pogonetsa kuti aone ngati angatsitsimuke. Ndinafunsa, "Zingatenge nthawi yayitali bwanji mmene mukuganizila kuti adzuke?" "Ndizovuta kudziwa bwinobwino," anatero "atha kudzuka lero, mawa, sabata ya mawa, mwezi wa mawa, chaka cha mawa, komanso atha osadzukanso," anamaliza.



Patapita masiku angapo, makina omwe amagwiritsa ntchito popuma anamuchotsa. Tinakondwera chifukwa anayamba kudzuka. Komabe, usiku Beatriz anapumira madzi mkatì ndipo mapumidwe ake anayipa. Mmene

tinafika ku chipatala, tinamuona akupuma movutika. Gulu la azachipatala linayesetsa kuchita chili chonse kumuthandiza kuti apeze bwino. Tinapita ku nkhomaliro, ndipo pamene tinabwelera ndikupempha kuti tilowe, anatiyimitsa. Ndinayanq'ana kudzera pa khomo ndipo pafupifupi gulu lonse linazungulira bedi lake likulira. Tinadikira kwa mphindi zambiri, ndipo nthawi yomwe anatilola kuti tilowe, tinaona kuti machubu opumila aja amuyikanso. Mmodzi mwa a dotolo anati "Mwina tigwiritsa ntchito njira yopumila kudzera mma chubu, ndipo Beatriz adzigwiritsa ntchito popuma mpweya kudzera mu chubu. Sangakwanitsenso kupuma mwaiye yekha." Nkhani inano yoipa—chifukwa china chopempherera. Patapita masiku angapo, Beatriz anatsitsimuka ndipo anapita kumalo ena osamalira odwala.

Tinapitiliza kumulirira Mulungu ndi kusala kudya nthawi zonse. Pamene Beatriz anapita ku malo ena osamalira odwala, tinasandutsa chipinda kukhala malo opempherera, maola 24 patsiku. Tinali ndi nyimbo zopembedza zimene timamvera. Timapemphera ola lililonse. Anthu amalowa ndi kuona Beatriz atagona pa bedi ali ndi mwendo okutidwa pulasitala, ataikidwa makina opumila ndi odyera ndipo amati, "Zikukhala bwanji kupeze ka mtendere malo ano?" Masiku omwe anagonekedwa m'chipatala onse anakwana 53.

Pamene Beatriz anatulutsidwa, anabwera kunyumba asakuonetsa zizindikiro zochira kwenikweni. Tinali ndi bedi ya kuchipatala, mpando osambira, ndi whilutcheya kunyumba. Mkazi wanga ankayankhula ndi dotolo wodziwa za matupi (physical therapist) ndipo anafunsa, "A dotolo, mukuganiza zitenga nthawi yaitali bwanji kuti Beatriz ayende?" Dotolo anayankha, "Ndakhala ndikugwira ntchito imeneyi kwa zaka zambiri, ndipo sindinapezeko m'mabuku azamankhwala kapena kumva nkhani ya aliyense kuti anapulumukapo ku ngozi ngati yomwe Beatriz anachita. Mwina tsiku lina adzakwanitsa kuyendera ndodo kapena choyendera,

koma kukwanitsa kuyenda bwinobwino—m'maganizo anga—sizidzathekanso." Komabe, tinalimbikitsidwa mu uzimu mwathu kuti sizidzamuthera choncho. Tinapitiliza kupemphera molimba kufuna Ambuye, nthawi zina muchikhulupiro, nthawi zina kulira, koma nthawi zonse kukhulupilira. Tsiku lina tinamutengera ku chipatala cha dera lomwe timakhala chifukwa tinkafuna chilolezo chopitila ku chipatala china, ndipo ndinamuza dotolo kuti zinali zachangu. Dotolo anapempha kuti amuone Beatriz, ndipo pamene ndinalowa mu ofesi ali mmanja mwanga, dotolo anafunsa, "Bambo ndichifukwa chiyani muli pachangu? Chingasinthe ndi chiyani ndi mmene alili mwanayu?"

Beatriz amayenera kuchitidwa sajare kuti amulowetse chinthu pomwe panachotsedwa fupa mu chigaza mwake. Tinayerekeza ndalamala (Real yaku Brazil) 147,500.00 (pafupifupi \$60,000.00 USD). Tinalibe ndalamayi, choncho tinali ndi chifukwa china choiti tipemphera. Titalandira malangizo kuchokera kwa Mulungu kudzera mwa mzathu, tinayamba kupanga kampeni yopezera ndalamala. Lachinayi lina, ndinalandira foni. Analu mzimai yemwe anayamba kufunsa za Beatriz. Anafunsa kuti ndi ndalamala zingati zimafunikabe, ndipo ndinati (BRL) 57,000.00 (\$23,000.00 USD). Anati awona ngati angachitepo kanthu za ife. Lolemba lotsatira, nditapita kukatapa ndalamala zotsala ku bank, ndinapeza kuti munthu uja anayikako ndalamala zomwe tinkafuna. M'masiku 40 tinakwanitsa kupeza ndalamala zonse zomwe timafuna. Ambuye alemekezeke!

Sajare inachitika pa 23 December 2011. Panthawi imeneyi, Beatriz anali akukwanitsa kukhala mothandizidwa ndi ma pilo ndiponso amatha kukhala pa whilutcheya. Pa 27 December, ndinapita kukamutsanzika Beatriz ndisanachoke kupita ku tchalichi. Ndinayamula manja ake ndipo ndinamuza kuti ndikupita ku tchalichi. Ndipo kenako ndinamva akundikoka dzanja langa. Ndinamugwira mwamphamu ndipo mwakamodzi anayimilira. Ndinachita mantha ndipo ndinabwerera mmbuyo, ndipo nthawi yomweyo,

anaponyanso sitepe kupita kutsogolo ndipo anapitiliza kuyenda. Mulungu ndiwokhulupilika!

Pamene masiku amapita, Beatriz anapitiliza kukhala bwino. Anayamba kuyankhula ndi kulemba. Mu May 2012, anabwelera ku sukulu.

Lero, patapita zaka zitatu, ndi mboni yamoyo ya mphamvu zodabwitsa, umboni woti Mulungu ndiwokhulupirika ku Mawu Ake ndipo amachita zokomera anthu ake onse okhulupilira. Mau omwe ndili nawo pa moyo wanu nthawi zonse ndi akuti, "CHILI CHONSE NDI CHOTHEKA KWA IYE AMENE AKHULUPILIRA" (Mariko 9:23).

Masiku ochepta apitawo, mkazi wanga anali ndi dotolo odziwa za matupi, ndipo dotolo ankamuwonetsa Beatriz kwa mmodzi mwa ophunzira ake ndikunena kuti, "(Izi ndizodabwitsa, chifukwa kupanda Mulungu, bwenzi yuu kulibe. Palibe chomwe mankhwala akanachita kwa iye."

Mankhwala palibe chomwe akanachita, koma MULUNGU ANGATHE! ATHA KUCHITANSO KU MOYO WANU.

M'busa Isaque Roberto

Umboniwu unaperekedwa ku tchalichi chonse ku Londrina ndipo wakhala chitsanzo cha mphamvu za Mulungu kuyesa chikhulupiliro chathu. Wonelani umboni omwe tinajambula ku tchalichi pa youtube: <http://www.youtube.com/watch?v=YHqbBk0A4nA>.

Cuba

(*Zomasuliridwa kuchoka mu Spanish*)
Moni kuchoka ku Cuba,

Mtendere wa Ambuye ukhale ndi aliyense. Tithokoze Ambuye, lero tinali ndi m'dalitso otenga maphukusi ena awiri.

Tithokozereni kwa atumiki onse a Mulungu omwe ali ndi mdalitso ofalitsa Mawu ku dziko lonse kudzera mu utumiki umenewu. Ndi-kuthokoza mwa padera kwa onse. Mulungu akudalitseni,
Reverend Marrero Havana, Cuba

NJIRA YOKHAYO YOCHOKERA

(Yachokera patsamba 4)

usiyeni mtima wanga ubweretse chikondi chimene sichidzakalamba. Landirani mbewu ya moyo wosatha. Yambani pakunena pemphero ili:

AMBUYE wanga komanso MULUNGU wanga, ndichitireni chifundo ndine munthu wochimwa.¹⁸ Ndikukhulupirira kuti YESU KHRISTU ndi MWANA wa MULUNGU wamoyo.¹⁹ Ndimak-hulupiriranso kuti IYE anafera pam-tanda ndipo anakhetsa mwazi WAKE wamtengo wapatali ndi cholinga choti machimo anga onse akhululukidwe.²⁰ Ndikukhulupiriranso kuti MULUNGU anaukitsa YESU kwa akufa pogwiritsa ntchito mphamvu ya MZIMU WO-YERA,²¹ ndiponso kuti IYE anakhala kudzanja lamanja la MULUNGU ndipo panopa akumva pemphero langa lolapali.²² Ndikutsegula zitseko za mtima wanga, ndipo ndikukuyitanani kuti mulowe mumtima mwanga, inu AM-BUYE YESU.²³ Tsukani machimo anga ambirimbiiri achoke onse mu mwazi wamtengo wapatali umene INU munakhetsa m'malo mwanga pamtanda wa ku Kavari.²⁴ Ndikudziwa kuti mundimvera pemphero langali AMBUYE

YESU; INU mukhululukira machimo anga ndi kupulumutsa moyo wanga. Ndikudziwa izi chifukwa MAWU ANU, Baibulo, limanena zimenezi.²⁵ MAWU ANU amati INUYO simudzakanaka kumvetsera pemphero la munthu ali-yense, ndipo ine ndili m'gulu la anthu amenewo.²⁶ Choncho, ndikudziwa kuti INUYO mukundimvetsera pamene ndikupemphera ndipo ndikudziwanso kuti INUYO mundiyankha komanso mundipulumutsa.²⁷ Ndipo ndikukuthokozani AMBUYE YESU, chifukwa chopulumutsa moyo wanga, ndipo ndisonyeza kuyamikira mwa kuchita zinthu zimene INUYO munalamula komanso kupewa kuchita uchimo.²⁸

Pambuyo pa chipulumutso, YESU ananena kuti munthu ayenera kubatizidwa pomizidwa thupilonse m'madzi, m'dzina la ATATE, ndi la MWANA, ndi la MZIMU WOYERA.²⁹ Muzip-hunzira mwakhama Baibulo la *Buku Lopatulika Ndilo Mau a Mulungu*, [King James Version] ndipo muzichita zimene Baibulolo limanena.³⁰

AMBUYE akufuna kuti inuyo muziwuza ena za chipulumutso chanu. Mungathe kukhala wofalitsa uthenga wabwino wa Mbusa Tony Alamo. Tizi-kutumizirani mabuku mwaulere. Im-bani foni kapena tumizani imelo kwa

ife kuti mudziwe zambiri. Tikukupem-phani kuti muwuzeko ena uthengawu.

Ngati mukufuna kuti dziko lipulumutsidwe monga m'mene YESU akulamulira, mukufunika kuperekwa chakhu-mi kwa MULUNGU. MULUNGU anati, "Kodi munthu angabere MULUNGU? Inde, mwandibera kale. Koma akuti, Ife tikumubera bwanji MULUNGU? Mu chakhumi ndi mu zopereka. Anthuwo ndi otembereredwa chifukwa akundibera, ngakhale mtundu wonsewu [dziko lonse lapansi]. Bweretsani nonse chakhumi ['chakhumi' ndi gawo limodzi la magawo khumi (10%) ya malipiro anu] m'nhokwe zanga n'cholinga choti pak-hale nyama [chakudya cha Uzimu] mu nyumba YANGA [anthu opulumutsidwa] kuti mundiyese, akutero AMBUYE wa MAKAMU, kuti muone ngati sindidzakutsegulirani mazenera a Kumwamba ndi kukukhuthulirani madalitso amene mudzasowa malo owalandirira." Ndipo ndidzadzudzula anthu okudyerani masuku pamutu ndipo sadzawononga zipatso za nthaka yanu; ngakhalenso mphesa wanu sudzalephera kubala zipatso pa nyengo yake m'minda yanu, watero AMBUYE wa MAKAMU. Ndipo mitundu yonse idzakutchani odala: chifukwa dziko lanu lidzakhala labwino, watero AMBUYE wa MAKAMU" (Malaki 3:8-12).

18 Sal. 51:5, Aro. 3:10-12, 23 19 Mat. 26:63-64, 27:54, Luka 1:30-33, Yoh. 9:35-37, Aro. 1:3-4 20 Mac. 4:12, 20:28, Aro. 3:25, 1 Yoh. 1:7, Chiv. 5:9 21 Sal. 16:9-10, Mat. 28:5-7, Marko 16:9, 12, 14, Yoh. 2:19, 21, 10:17-18, 11:25, Mac. 2:24, 3:15, Aro. 8:11, 1 Akor. 15:3-7 22 Luka 22:69, Mac. 2:25-36, Aheb. 10:12-13 23 1 Akor. 3:16, Chiv. 3:20 24 Aef. 2:13-22, Aheb. 9:22, 13:12, 20-21, 1 Yoh. 1:7, Chiv. 1:5, 7:14 25 Mat. 26:28, Mac. 2:21, 4:12, Aef. 1:7, Akor. 1:14 26 Mat. 21:22, Yoh. 6:35, 37-40, Aro. 10:13 27 Aheb. 11:6 28 Yoh. 5:14, 8:11, Aro. 6:4, 1 Akor. 15:10, Chiv. 7:14, 22:14 29 Mat. 28:18-20, Yoh. 3:5, Mac. 2:38, 19:3-5 30 Deut. 4:29, 13:4, 26:16, Yos. 1:8, 22:5, 2 Tim. 2:15, 3:14-17, Yak. 1:22-25, Chiv. 3:18

Ngati mukufuna kudziwa zambiri kapena ngati mukufuna mabuku kapenanso nkhanizina zimene zimakusangalatsani, tiimbirenifoni kapena tilembereni.

Tony Alamo, World Pastor, Tony Alamo Christian Ministries Worldwide • P.O. Box 2948, Hollywood, CA 90078

Twenty-four hour prayer and information line: (661) 252-5686 • Fax (661) 252-4362

www.alamoministries.com • info@alamoministries.com

Tony Alamo Christian Ministries Worldwide imalandira anthu onse ndipo imaperekazinthu zofunkika Kwa onse amene ali ku U.S. amene akufunitsitsadi kuti ayambe kutumikira AMBUYE ndi mtima wawo wonse moyo wawo wonse ndi mphamvu zavo zonse

Maservice amachitikira ku New York City lachiwiri lililonse nthawi ya 8 koloko usiku ndi malo ena usiku okhaokha.

Chonde imbanu (908) 937-5723 kuti mudziwe zambiri. ZAKUDYA ZIMAGAWIDWA PAMAPETO PA MAPEMPHERO ALIWONSE.

Funsani buku la M'busa Alamo, lakuti Mesiya, losonyeza KHRISTU kuyambira ku Chipangano Chakale mu maulosi oposa 333.

**Khalani wogwira ntchito yokolola miyoyo ya anthu pakukhala ogawira mabuku a M'busa Alamo
Mabuku ndi zinthu zonse zomvetsera n'zaulere, ndipo simulipira ndalamaya yotumizira**

Ngati wina akukuuzani kuti mupereke ndalamaya pa zinthu zimenezi, chonde imbanu pa (661) 252-5686.

**M'BUKU ILI MULI CHIKONZERO CHENICHENI CHA CHIPULUMUTSO (Machitidwe 4:12).
MUSALITAYE, PATSANI ENA KUTI AWERENGE.**

**Anthu amene muli m'mayiko ena, tikukulimbikitsani kuti mumasulire n'chinenero chanu mabukuwa. Ngati
mukusindikizanso bukuli, musaiwale kuika mawu ali m'munsiwa omwe ndi okhudzana ndi zamalamulo:**